


Maziko Olimba

Kumanga umoyo wanu pa nchito yomwe khristu adasiliza

Ndi

Ken Legg, Australia



Copyright © Ken Legg, 2014

www.kenlegg.com.au

Maphunziro awa angapangidwetso ndi kupatsidwa kwa ena (ndi osagulitsa) kulingana ndi ndanga la kuyapangatso inapatsidwa moyenera ndi zolembedwa pa tsamba ili.

Maziko Olimba

Kuyamika koono ,kwa Michael John Phiri, emwe adasaduliza buku la Maziko Olimba mcinyanja kuti cisomo ca Mulungu cimvetseseke mu citundu coziwika bwino mdera lathu. Nchito yabwino Michael John Phiri. Masopenya ako ndi kulimbikira kusiliza nchito iyi , zizabereka zipatso mu nthawi iri kubwera .

Matamando a padera kwa Dorica Zulu Mulyata paku thandizira ku sanduliza . Cynthia Tembo, Edina Lungu, Paul Daka, Obrin Zulu, ndi Pangu Chanda pakupitamo zo sandulizazo . Joseph Mulyata pakuyanganira ndi kulongosola nchito iyi. Kuseweza kwanu mu cikondi kuzapasidwa phaso ndi Ambuye.

1) MAZIKO A ATUMWI

- ✓ Cinthu cofunikira kwambiri pa zomangidwa, ndi Maziko. Ici ndi cimodzi modzi ndi mpingo.
- ✓ Maziko amaonesera malekezero ndi kaonekedwe ka comangidwa.
- ✓ Nchito yaikulu ya Atumwi ndi kuika Maziko. 'Tinamangidwa pa maziko a Atumwi ndi Aneneri, Yesu Khristu Kukhala ngati mwala wapangodya.' (**Aef. 2:20**).
- ✓ Maziko ndi Yesu, **1 Akor. 3:11**. Tifunika kuzika mizu ndi kukhalabe mwa Iye.
- ✓ Atumwi 12 adaphunzitsidwa ndi Yesu zaka zitatu. Ici ciphunzitso cidaziwika kuti ndi ciphunzitso ca Atumwi, comwe akaphunzitsa mpingo ngati maziko.

Paulo adali mtumwi kwa akunja (Agal. 1:11 ndi 12)

- ✓ Monga mwamene Yesu adaphunzitsa ophinzira ace zaka zitatu, adaphunzitsanso Paulo mwo mangira mupingo.
- ✓ Ngati womanga wanzeru adaika maziko wa ku mipingo, **1 Akor. 3:10-11**.
- ✓ Adali naco coonadi comwe adaphunzitsa mofikapo ndi momvetseka kumipingo.
- ✓ Adacha ici kaonekedwe ka ciphunzitso. Kwa Aroma adalemba akuti 'Mudamverera kucoka mumtima mwanu kaonekedwe ka ciphunzitso comwe cidakuombolani', (**Aroma 6:17**).
- ✓ Liu kutembenezidwa lakuti 'kuomboledwa' lithantauza kupatsidwa kucinthu kapena kwa wina.
- ✓ Pansi pa cipangano ciliconse Anthu a Mulungu adali kupatsidwa kwa kuciphunzitso ca cipanganoco.
- ✓ Pamene Mose ana seluka pa luphiri ndi malamulo khumi, sana peleke cabe malamulo kwa ana a isreali komanso ana peleka ana a isreali ku malamulo.
- ✓ Iwo adali pansi pa cipangano cakale adali 'nazo nzeru ndi coonadi ca lamulo' (**Aroma. 2:20**).
- ✓ Mulungu anali kucitila Anthu amu cipangano cakale kulingana ndi lamulo. Aya ndiyo anali.
- ✓ Kunena za nthawi imeneyi Paulo anena kuti 'tindasungidwa pansi pa lamulo' (**Agal. 3:23**)
- ✓ Koma Pamene timvera ndi ku khulupirira mu uthenga wa bwino tiomboledwa ku lamulo ndiku patsidwa ku ciphunzitso ca Atumwi. Paulo ananena kuti tinaomboledwa ndiku patsidwa ku ciphunzitso ca Atumwi (**Aroma 7:6**)
- ✓ Ciphunzitso ca Paulo cidaonesedwa mdime yapakati yoyamba ya Aroma 6 ilankhula pa ubatizo wathu mu imfa ya Khristu, kuikidwa m'manda, ndi kuukisidwa.
- ✓ Uyu ndiye uthenga wa bwino (**onani Akorinto 15:1-4**). Yesu sa nafe, kuikidwa, ndi kuutsidwa cabe, cifukwa ca ise, komanso ise tinafa ndi kuikidwa ndi kuutsidwa naye mu umoyo wa tsopano.
- ✓ Pakugwirizana ndiye tina matsuridwa ku maonekedwe amu cipangano cakale ndiku patsidwa ku ciphunzitso ca Atumwi mu cipangano ca tsopano.
- ✓ Tikakhulupirira, umoyo wanthu ukhala bwino cifukwa ca izi.
- ✓ Pakugwirizana ndi Yesu timamvera ubwino wa imfa yake ndiponso mphamvu za kuukisidwa kwa umoyo wake. Ndiwo umoyo woona wa Mkhristu.

Ndondomeko ya mau omveka bwino

- ✓ Ciphunzitso ca Atumwi cionesedwa ndi 'ndondomeko ya mau abwino', mwacitsanzo mau odziwika bwino womwe akakhulupiridwa akonza umoyo wa wokhulupirira ndi mpingo. Paulo adauza Timoteo kuti: 'Ugwirisitse mau abwino womwe adamva kwa ine' (**2 Tim. 1:13**).
- ✓ Tina patsidwa ku maphunzitso a mau omveka.
- ✓ Yena mwa mau abwino yomwe Paulo adali kusewezetsa adali: cilungamo, mwa Khristu, Cikhulupiriro, ana a Mulungu, mbadwo, cipangano catsopano, Mzimu, munthu watsopano, cikondi ca Mulungu, umoyo wamuyayaya, ndi zina zotere.
- ✓ Aya mau omveka tikayagwiriritsa adazatsogolelamyoyo zanthu.
- ✓ Mau aci Greek onena kumveka athathauza moyo wa khoma. Maphunzitso okhoma amaleta umoyo wokhoma.

Kukazikisidwa pa mau otsamveka amaphunziro a munthu

- ✓ Ngati sitindakazikisidwe pa ciphunzitso ca Atumwi ndiye kuti tili okhala mu ciphunzitso ca anthu.
- ✓ Comwe cionesedwa ndi makambidwe a anthu amaphempezo omwe ali pozungulira pokhala.
- ✓ Muku siyana ndi mau omveka omwe Paulo ada phunzitsa, aya mau otsamveka bwino anena za mphamvu zanthu ndi acilwendo mu cipangano catsopano.
- ✓ Ndipo yoamveka bwino abweretsa zabodza ndi maganizo osowetsa mu umoyo wa Cikhristu.
- ✓ Mwachitsanzo, ena mwa mau osewzesedwa mu zipembedzo ndi: panga sankho kapena ulimbikireso, pereka mtengo, limbika, kupeza zanthu, njira 4..., masomphenya, fikapo, bzala nzeru, ndi zina zotero.

Zomwe Paulo adali kukonkha po manga mpingo

- ✓ Coyamba adali kuphunzitsa coonadi cimeneci kwa anthu osakila ngati Timoteo ndi Tito.
- ✓ Ndipo ankawauza kuti aphunzitse zimenezi kwa atsogoleri omwe adayamba kuphunzitsanso mumpingo yao.
- ✓ Mwachitsanzo: Adati kwa Timoteo, 'zinthu Zomwe udamva kwa ine pakati pa mboni zambiri zokhulupirika, zimenezi uziphunzitse anthu okhulupirika omwe adzaphunzitsa enaso' (**2 Tim. 2:2**).
- ✓ Anati kwa Tito, mkulu wa mpingi agwiritsitse 'mau okhulupirika omwe adaphunzitsidwa, kuti akwaniritse, mwa ciphunzitso cibwino, akweze ndi kukutiritsa iwo otsutsa' (**2 Tito 1:9**).
- ✓ Ngati iwo opanga Atumwi sadaphunzitsidwe bwino iwo, azakhala atsogoleri a akungu azao.
- ✓ Uku kudziwa kuphunzitsa sikufunikira munthu olankhula pakati pa anthu, kapena olalikira mumpingo, koma akulu ampingo afunikira kuphunzitsa kapena kutsogolera anthu pakulankhuzana nao wina ndi wina mu mau abwino a maziko a Atumwi.

Zokambirana

1. Kodi cithantauzanj ikuzika mizu ndi kukhazikika mwa Khristu?
2. Kodi kugwirizana ndi Khristu mu imfa yace, kuikidwa m'manda ndi kuuka kwace kutanthauzani kwa iwe?
3. Pomwe udapulumsidwa kodi udapatsidwa kuziphunzitso za Atumwi kapena kaziphunzitso zopangidwa ndi anthu?
4. Ngati udakhala momwe ulili cifukwa ca ziphunzitso za anthu kodi ndi mau ofunikira otani yomwe yanali kusewzedwa pa mkhalidwe uja yomwe udziwa kuti siyanali mumalemba ndiponso ndiyosathandiza?
5. Kodi ni kofunikira kotani kumasulidwa kumalamulo ndi zovomelezeka zacipembezo?
6. Kodi ndi mau yoti ya Atumwi pa ndondomeko yali yomveka bwino kwa iwe? Kodi ungaganizirepo mau ena ofunikira kuwonjezerapo Zomwe Atumwi adaphunzitsa?
7. Kambilanani Nchito ya Mzimu Woyera pakuti ife timvetsetse coonadi?

2) CILUNGAMO

‘...Iwo olandira kuculuka kwa chisomo, ndi m’phatso ya cilungamo adzalandira ndi m’modziyo Yesu Khristu **(Aroma 5:17)**

- ✓ Kupyolela mwa caulele ca cilungamo ndi ku culuka kwa cisomo ca Mulungu kwa ise mwa Khristu ti kwanilisa kulamulira mu umoyo.
- ✓ Ngati Satana angakwaniritse kuticotsa kucoonadi ca cilungamo ndi cisomo, angakwanitsenso kutileperetsa kulowa mdalitso iliyonse.

Mcigawo ici, tizaona momwe cipangano catsopano ciphunzitsa pa cilungamo.

Abraham ndiye citsanzo cathu.

- ✓ Abraham acedwa “Tate wa onse” **(Aroma 4:16)** ndipo ndicitsanzo ca cibwenzi ndi Mulungu.
- ✓ Ndi munjira yotani mwamene anali citsanzo keaise? Kodi tiyese Kukhala monga mwamene iye anankhalila?
- ✓ Ai. Adasokoneza dzinthu zambiri, koma adakwaniritsa cinthu cofunikira kwambiri. Adali naco civumbulitsa kuti njira ya Mulungu yacilungamo idzera mwa Yesu.
- ✓ Mulungu anamulonjeza kuti kupyolera mwa mbeu yake, maiko ambiri azakadalitsidwa.
- ✓ Abraham adamvetsetsa kweni kweni kuti mbeu yo ndi Yesu Khristu. “Ndipo mulonjezano ananenedwa kwa Abraham ndi kwa mbeu yace. Sana nene ndipo kwa zimbeu, ngati Kunena zambiri: Komatu ngati Kunena imodzi, ndipo kwa mbeu yako ndiye Khristu” **Agalatiya 3:16**
- ✓ Mulungu analalikirira uthenga wabwino kwa Abraham “Ndipo Mulungu pakuoneratu kuti Mulungu adzayeresa olungama amitundu ndi Cikhulupiriro adayamba kale kulalikirira uthenga wabwino kwa Abraham, kuti idzadalitsidwe mwa iye mitundu yonse.” **(Agalatiya 3:8)**. Yesu anati kwa Yuda “Atate wanu Abraham anakondwera kuona tsiku langa, ndipo anaona nasangalala” **(Yohani 8:56)**.
- ✓ Abraham adakhulupirira uthenga wabwino wamene tina khulupirira na ise.
- ✓ Paku khulupirira uthenga wabwino wa Yesu Khristu Mulungu Anamuona kuti ni olungama. “Abraham anakhulupirira Mulungu, ndipo cinawerengedwa kwa iye cilungamo” **(Aroma 4:3)**, monga mwamene tilili ife.

Kusinthanisa kwa kukulu

Cilungamo ca Mulungu ndiye ciyanbi ca cibwenzi cathu ndi Mulungu. Cimatifikiriza pa zinthu zones zabwino.

Kumakhalpo ‘kusinthanitsa kwakukulu’, **(2 Akor 5:21)**. Izi zitanthauza:

A) Mulungu aika macimo athu pa Yesu (Aroma 4:7 ndi 8)

- ✓ Davide adacimwa macimo awiri osakhululukidwa, koma siyandaikidwe pa iye.
- ✓ Mulungu alungamitsa osalungama, **(Aroma 4:5)**. Kodi angazicite bwanji zimenezi?
- ✓ Macimo athu adapatsidwa kwa Yesu. Adapilira ciweruzo conse.
- ✓ Pa mtsinje wa Yodani, Yesu adaonetsa kuti adzakwaniritsa cilungamo conse, **(Mat. 3:15)**.
- ✓ Mu ubatizo adaonetsa Zomwe zikacitika pamtanda. Adaimirira mbadwo wa mtundu wo cimwa, kufera macimo awo, kuikidwa m’manda ndi kuukidwa ngati mkulu wa mbadwo wa tsopano.
- ✓ Comweco, macimo athu onse, akhale, tsopano, angakhale apatsogolo, adapatsidwa pa iye, **(Yohane 12:31-32)**

B) Mulungu aika cilungamo ca Yesu pa ise (Aroma 4:6)

- ✓ Ayuda sanadziwe njira ya cilungamo ca Mulungu motero, anaganidza kuti angakhale oyera Kupyolela mukutsatira malamulo. “Pakuti pakusadziwa cilungamo ca Mulungu ndipo pakufuna kukhazikisa cilungamo ca iwo okha, iwo sanagonje ku cilungamo ca Mulungu” **(Aroma 10:3)**. Anthu ambiri akali kupanga uyu mtsokonezo.
- ✓ Sitalungamitsidwa cifukwa caku mverera kwatu...cifukwa ca kusamvera kwa munthu umodziu, anthu adasanduka osalungama, cifukwa ca kumverera kwa munthu winanso umodzi, ambiri apezeka kuti ngolungama” **(Aroma 5:19)**
- ✓ Sitionetsera mum’khalidwe kuti tili olungama, komatikhulupirira kucilungamo.

Wakayere Kapena Olungama

Maziko adalitso ndiye kukhala naco cibwenzi coonadi ndi Mulungu. Adamu adadalitsidwa Pomwe adali pa cibwenzi ndi Mulungu. Koma Adamva kuwawa kwa tembelero atacimwa. Sitili muli Adamu (waponda maindu kufikira utapezedwa nawo), koma muli Yesu (Olungama) anga khale tacimwa.

Pali kusiyana pokhala wopanda mulandu ndi wolungama:

- ✓ Pomwe munthu wopanda mulandu acimwa, cimo limabwera pa iye.
- ✓ Pomwe munthu wolungama acimwa, cimo limabwera kwa Yesu. **(Onani Aroma4:8)**
- ✓ '...Mulungu mwa Khristu ankhayanjanitsa anthu a pa dziko lonse lapansi kwa iye Mwine, osawerengera macimo awo...' **(2 Akor. 5:19)**
- ✓ 'Mwacifundo, ndizawa khululukira zocimwa zao, sindidza kkumbukiranso macimo awo' **(Aheb. 8:12)**

Citsanzo Coyamba. **Gen. 12:10-20; 13:1-2.**

Ndani adacimwa?

Ndani adazuzulidwa ndi Mulungu?

Ndani wamene Mulungu adadalitsa?

Citsanzo caciwiri. **Gen 20:2-7; 14-16.**

Ndani adacimwa?

Ndani wamene Mulungu adacenjeza?

Ndani wamene Mulungu adadalitsa?

Mulungu adadalitsa Abraham olo atacimwa cifukwa anali olungama cifukwa ca ci khulupirira mwa Yesu Khristu. Uyu simphatawo cimwa. Ocimwa amalangidwa nthawi zones. Koma Mulungu amati dalitsa cifukwa ca cilungamo cathu mwa Yesu Khristu, osati cifukwa cama citidwe athu.

Zokambirana

1. Kodi paliko nthawi ina mu kuyenda mu ci Khristu cako Pomwe udaganizira kuti uyenera kapena suyenera pa madalitso ndi cifundo ca Mulungu kulingana ndi mkhalidwe wako?
2. Kodi ukhulupirira kuti macimo ako onse – akumbuyo, yatsopano ndi kutsogolo – adakhululukidwa khale?
3. Kodi kunga khale Mkhristu amene ali wolungama kupambana wina?
4. Kodi unga muuze ciani Mkhristu omwe akhulupirira kuti cilungamo cake cikhalapo cifukwa ca ku mverera kwake?
5. Kambiranani pazotulukamo pa ncito yomwe Khristu adamaliza. Kodi Yesu adatanthauzanji Pomwe dati adzakwaniritsa cilungamo conse? Ndipo ndi ciani adatanthauza Pomwe adalira pamtanda “kwathaa”!?
6. Kodi uthenga uyu wabwino umakupangisa kuti ucimwe kwambiri, mwina umakupangisa kuti ukonde Mulungu kwambiri?

3) KUDZIWIKA

Funso lofunikira ndi ili, 'kodi ndine yani?'

Mwacisoni A Khristu ambiri alandira uthenga wa kudziwika kwao kucokera kuziphunzitsa zonama. Mwacitsanzo:

- ✓ Zokwaniritsa
- ✓ Kulankhulapo mau
- ✓ Maonekedwe
- ✓ Mkhalidwe

Ndiwe yani?

Ngati Akhristu sitilandira kudziwika kucokera mu Zokwaniritsa, mkhalidwe kapena maonekedwe, osatinso kulankhulapo mau ena kapena kusalankhulapo kwa ena.

Kudziwika kwathu kuli pa iye yomwe tima dziwikirako.

Aroma 5:12-21 inena kuti:

- ✓ Tinali anthu a 'mwa Adamu'
- ✓ Tsopano tili anthu a 'mwa Khristu'

Paulo momwe anakondwera kunenera za Mkhristu ndi wina ali 'mwa Khristu'

Kumvetsetsa kudziwika kwa mbadwo watsopano nicofunikira kuumoyo wabwino wauzimu, cifukwa sozomwe timacita zionetsera kuti ndise Ndani, koma kudziwa kuti ndise Ndani zizaonesera Zomwe timacita.

Bongo wathu uzapereka umoyo wathu mwamene tiziganizira tseka.

Bvuto yomwe Akhristu alimbana nayo ndi iyi: Alinako kudziwika kwa tsopano, koma maganizo akali akhale.

Kucoka kukaganizidwe mwa khale kufika kudziwika ndi maganizo atsopano.

Timacoka kukaganizidwe kakudziwika mwa khale kufika kudziwika ndi maganizo atsopano pakusinthana maganizo athu.

Mu **Aroma 6:1-14** Paulo agawana nafe njira ziri 4 motero:

- 1) Aroma 6:3-4.** Dziwani kuti mudafa kukadziwikidwe ka mwa Adamu ndipo mudaukisiridwa ndi mbadwo wa tsopano kukhalapo kudziwika kwatsopano mwa Khristu.
 - ✓ Coonadi ndico cidzatimatsula
 - ✓ Boza ndiya mphamvu imodzi cabe ali nayo Satana. Amalengesa munthu kukhala kapolo aka khulupilira boza lake.
 - ✓ Cofunikira si kukumana ndi mphamvu, koma kukumana ndi coonadi.
- 2) Aroma 6:8.** Khulupilirani kuti ndinu mbadwo wa tsopano mwa Khristu.
 - ✓ Sikudziwa coonadi coka cimene cifunika, koma tiyenera kukhulupilira.
 - ✓ Akhristu ena ndi osa khulupilira
- 3) Aroma 6:11.** Zindikirani kuti ziri tere, kutanthauza kukhala mofunikira.
 - ✓ Kudzindikira ndi nkuthenga coonadi cathu ndi kukhala motere.
- 4) Aroma 6:13.** Perekani ziwalo za mathupi anu kukhala zitsulo za cilungamo.
 - ✓ Mkhristu ali ndi mbadwo wa tsopano wamene unkhala muthupi la khale. Thupi limene tilinayo ndilo thupi lamene Tinali nalo tikalibe ku pulumutsidwa.
 - ✓ Khale tinali kumverera cifuniro ca thupi, koma manje tamatsulidwa ku mphamvu ya ucima.
 - ✓ Tinga sanke kupereka ziwalo za mathupi atu kukhala zitsulo za cilungamo.

Zokambirana

1. Kodi uthenga wakuzidzidziwa umautenga kuti?
2. Kambiranani mau awa 'sizomwe ticita zomwe zionetsera kuti nditse ndani , koma kudziwa kuti nditse ndani zionetsera zomwe ticita'
3. Kodi udziwa kufika poti kuti udfa mkudziwika 'mwa adam ' ndipo uli mcilengedwe catsopano 'mwa khristu'?
4. Kodi ndi zotulukamo zina zontani zili mwa ici coonadi?
5. Kodi ndi cifukwa ciani okhulupirira ena akali ndi maganizo akale pa zakudziwika kwao ? kodi ndi ciani cidzathandiza kuti akhale ndi maganizo atsopano pa kudziwika mu mbadwo watsopano?
6. Kambiranani ndondomeko zinai zakupangatso maganizo atsopano . Gawanani ulendo wanu mwa ici .kodi uli pati mndondomeko iyi manje?

4) CIKUMBUMTIMA CACILUNGAMO

- ✓ Nsalu mchihema ndiye cithunzi coteteza coona comwe cilempheresa ise kumva ubwino wa kukhalapo ndi dalitso la mulungu, mwacitsanzo. Cikumbumtima ca ucimo, **Aheberi 9:7-8**
- ✓ Masiku yano kulibe temphere, ndiponso njira yobwera pa manso ya mulungu ndiyo tseguka koma anthu ambiri satengamo
- ✓ Nyula ya ma temphere ndi cithunzi-thunzi ca cinthu cimene cimati patula pa manso a Mulungu ie. Cikumbumtima caucimo. “Ndico ciphiphiriso ca ku nthawi yomwei m’mene mitulo ndi nsembeso zinaperekedwa zosakhoza ponena za Cikumbumtima yesa wangwiro wolambirayo” **Aheberi 9:9**
- ✓ Anthu adapanga njira zosokoneza zofuna kulimbanandi ucimo, mwacitsanzo: kuthawa Mulungu, kunenezera ena, kukana, kuzipatsa mlandu, kumvetsa cisoni, kukwinyirira, ndi zina zotere.
- ✓ Zodziwika bwino pakuonetsa Cikumbumtima colakwa ndi kucita ncito zopereka ‘kuifa’ izi ndiye ncito za kufa.
- ✓ Yankho ya Mulungu ku Cikumbumtima caucimo ndi cilungamo kupyolera mumwazi wa Yesu Khristu, “Koposa kotani nanga mwazi wa Khristu wamene anadzipereka yekha wopanda cirema kwa Mulungu mwa mzimu wosatha, udza yeretsa Cikumbumtima canu kucisiyanitsa ndi ncito zakufa kukatumikira mulungu wamoyo” **Aheb. 9:14**
- ✓ Kuziwa kuti cilungamocathu cibwera kupitila muku yanjana kwatu ndi Mulungu.
- ✓ Iwo osaphunzira bwino mau a cilungamo amanenedwa akhanda. “Pakuti yense wakudya mukaka alibe cizolowezi ca mau a cilungamo; pakuti ali khanda.” **(Aheb. 5:13)**. Coyamba mu kukura kwati mwa Khristu ndi kudziwa kuti macimo athu onse akhululukidwa. Ndipo sitikhalanso akhanda koma ana. **(1 Yohane 2:12a)**
- ✓ Tilimbitsidwa kuti tifike pa ‘kukhala opanda kalema’ kupyolera pa kutembenuka kucita zosapindulitsa ndi kuoneretsa Cikhulupiriro mu mwazi wa Yesu. ‘Tsono tisangoima pa maphunziro oyamba eni eni aKhristu. Tisacite kubweranso kuphunzitsa Zomwe zili ngati maziko, ngati za kutembenuka mtima kusiya ncito zosapindulitsa moyo osatha, za kukhulupirira Mulungu’ **(Aheb. 6:1)**
- ✓ Mau akhuti kukhala ‘opanda kalema’ atanthauza kuti kubweretsa cinthu kufikapo pa cofunikira comwe cindalengedwera. Tindalengedwa kulankhudzana ndi Mulungu.

Kuti tikhale mum’khalidwe opanda kalema ncofunikira kuti:

A) Tikhutire kuti Mulungu alibe Cikumbumtima ca macimo anthu.

B) Tilibe Cikumbumtima ca macimo anthu, koma tili nako kudziwa kwakukulu kokhala olungama.

A) Mulungu sakumbukiranso macimo athu

- ✓ Cipangano catsopano ndi cipangano cabwino comwe cili ndi malonjezo abwino, **Aheb. 8:6 ndi 7**
- ✓ Kupyolera muifa ya Yesu macimo athu onse adacotsedwa muyaya pamaso pa Mulungu ndi m’maganzizo ake. ‘Mwacifundo ndi dzakhululukira zocimwa zao, sindidza kumbukiranso macimo ao.’ **Aheb. 8:12**.
- ✓ Kumwamba kudafafanizidwa za ucimo wathu, **Aheb 9:23-26**.
- ✓ Kwa okhulupirira, Yesu emwe abwera salankhulapo pa ucimo. ‘Munthu aliyense amafa kamodzi kokha, pambuyo pake nkumawerudzidwa, momwenso Khristu adaperekedwa nsembe kamodzi kokha, kuti asenze ndi kucotsa macimo a anthu ambiri. Adzaonekanso kaciwiri osati kuti adzacotseso ucimo ai, koma kuti adzapulumutse anthu amene akumuyembekeza’ **(Aheb 9:27-28)**.
- ✓ Mulungu sapatsa mlandu wokhulupirira.

B) Tilibe Cikumbumtima ca ucimo wathu, koma ca cilungamo cathu

- ✓ Maganzizo a mumtima wathu amalankhula naise pa mkhalidwe wathu.
- ✓ Koma maganzizowo angalankhule zoon ngati yadauzidwa zoon.
- ✓ Ncito ya cikumbumtima ndi kulankhula ndi ise, ncito ya mwazi ndi kulankhula kwa Mulungu. ‘Koma inu mwafika ku Phiri la ziyoni, ndiponso ku mzinda wa Mulungu wamoyo, ndiye kuti Yerusalemu wa Kumwamba, m’mene muli angelo osawerengeka. Mwafika kuci kondwerero kumene kwasonkhana ana oyamba a Mulungu, amene maina ao adalembedwa Kumwamba. Mwafika kwa Mulungu, mweruzi wa anthu onse, ndiponso kwa mizimu ya anthu alungama, amene Mulunguna wawasandutsa angwiro kweni-kweni. Mwafika okhetsedwa, amene akutilonjeza zinthu zabwino Koposa m’mene mwazi wa Abele’ **(Aheb. 12:22-24)**

- ✓ Ngati Cikumbumtima cathu ndi cofoka ndipo cosaphunzitsidwa, Mulungu apambana mitima yathu. ‘Nthawi zones Pamene mtima wathu ukutitsutsa kuti ndife olakwa. Paja Mulungu ndi wamkulu kupambana mtima wathu, ndipo amadziwa zonse’ **(1 Yohane 3:20)**
- ✓ Mdierekezi ndi woneneza abale. Asewendzetsa zipembedzo pa lingo limeneli. Zipembedzo ziti kumbutsa ucimo. Ici ticionera mu cipangano cakale mwamene anali kubwezapo kupereka nsembe. Ici cinali kuwa kumbutsa cimo.
- ✓ “Pakuti cilamulo pokhala nao mthunzi wa zokoma zirikudza, osati cifuniziro ceni-ceni ca zinthuzo sicikho zatu, ndi nsembe zomwezi caka ndi caka, zimene azipereka kosalekeza, kuwayesera angwiwo akuyandikira. Pakadapanda kutero, kodi sakadaleka kuzi pereka, cifukwa otumikirawo sakadankhala naco Cikumbumtima ca macimo...” **(Aheb 10:1-3)**.
- ✓ Bvuto limeneli lipezeka ngati Mkhristu akhala wo kumbukira cimo.
- ✓ Cipembezo citi kumbukitsa macimo, koma mulungu aiwala macimo, cipulumutso cake cicosa macimo Pamodzi ndi Cikumbumtima. Koma iye m’mene adapereka nsembe imodzi cifukwa ca macimo, anankhala pa dzanja la manja ya Mulungu cikhali...pakuti ndi cipereko cimodzi anawayeretsa angwiwo cikhaliweyo oyeretsedwa. **Aheb 10:12 ndi 14**
- ✓ Mzimu Woyera satikumbukitsa pa macimo, koma pa cilungamo. “Koma mzimu woyeranso ati citira umboni, pakuti adathakunena ici ndi cipangano ndidzipangana nao, atapita Masiku ajawo, anena ambuye ndi dzapereka malamulo anga akhale pamutima pao, ndipo pa nzeru zao ndi dzawalemba...” **Aheb. 10:15-17**
- ✓ Iye ndiye Nkhoswe. Acitira umboni kuti ndise ana, ndi olamulira. “Pakuti inu simunalandira mzimu wa ukapolo kucitanso mantha, koma munalandira mzimu wa umwana, umene tipfuula nao, kuti, abba, atate. Mzimu yekha acita umboni Pamodzi ndi mzimu wathu kuti ndise ana a Mulungu” **Aroma 8:15-16**
- ✓ Mzimu Woyera adapatsidwa kwa ise kutisonyeza zinthu Zomwe zidapatsidwa mwaulele kwa ise mwa Khristu. **(onani 1 Akorinto 2:-12)**

Zokambirana

1. Pomwe adakhala Mkhristu kodi umavutika ndi kuganizira kuti ndiwe wolakwa? Kodi udayetsetsa kuthetsa bwanji iyi Bvuto?
2. Ngati sitinadziwe ciphunzitsa ca cilungamo kupyolera mcikhulupiriro mwa Khristu tizapedza Bvuto kuyenda patsogolo muumoyo wa Cikhristu. Kodi izi mudzipitamo pa nthawi ina yace? Ndiliti ndiponso ndi bwanji Pomwe civumbulitsa ca cilungamo cidabwera kwa iwe?
3. Kodi ubvomeredza kuti Mulungu sakumbukiratsa macimo ako? Kodi ukhulupirira kuti Yesu akazabwera sazalanxhulanso pa macimo ako?
4. Ndi njira iti yomwe Cikumbumtima cathu cinganamidwe, ndipo cayamba ndi kukumbukira macimo cabe?
5. Kodi ukhulupirira kuti ufunikira kulapa macimo Pomwe yakalibe kukhululukiridwa?
6. Kodi ndi njira iti yomwe wamvetsetsa ncito ya mzimu Woyera – Yemwe amauza ndi kukhutiritsa a Khristu pa cimo, kapena iye yemwe amawauza pa za cilungamo cao ndiponso pa za kukhala ana a Mulungu?

5) CISOMO

‘...Iwo olandira kuculuka kwa cisomo ndi mphatso ya cilungamo adzalamulira mu umoyo ndi yekhayo, Yesu Khristu’
(Aroma 5:17)

Cisomo ndiye comwe cimasiyanitsa ci Khristu. Ndi momwe Mulungu amayanjana ndi ise m’cipangano catsopano. Satana ayesa kusewezetsa cipembezo kuti asitanitsecisomo ndi zinthu zobvomeredzedwa cabe.

- ✓ Zobvomeredzedwa ndi zokhulupirira kuti ncito zanga ndiye ciyambi cakuti Mulungu wabvomeredza ndiponso wandidalitsa. Zooni ndi za paiwe cabe.
- ✓ Cisomo ndi cikhulupiriro kuti nthawi zonse ndine wobvomeredzedwa ndi wofikapo pa dalitso iliyonse cifukwa ca ncito adasiriza kale Yesu. Zoonapo ndi Yesu.

Zobvomeredzedwa

- ✓ Zobvomeredzedwa zimaticotsa komwe kuli mtanda. Zitiyesetsa kuti tipereke mtengo pa Zomwe Mulungu adatilipirira. Zisewezetsa lamulo pa lingoli.
- ✓ Baibulo lisewezetsa liu lakuti ‘lamulo’ kutionetsa kuti ndi lamulo tingacite kuti ndi lamulo la Mose. Koma likamasewezetsa liu loti ‘lamulo’ limaimirira ncito zobvomeredzedwa zonse zimene tingacite kuti Mulungu ati mverera cifundo, kapena momwe tingayesere kusintha.
- ✓ **Aroma 7:1-4**. Cipangano catsopano sicitsutsana ndi lamulo, koma pa kukwatiriwa kwa icho. Pakugwirizana ndi Yesu tidamwalira ku lamulo kuti tikwatiwe kwa Yesu. Ndiye ciyambi ca ciyero cathu. Mwa Yesu Khristu Tilibe lamulo, koma umoyo.

Zosokoneza pa lamulo ndi Cisomo

1. ‘Lamulo izandithandiza kuti ndi khale na umoyo wabwino’

- ✓ Paulo adanamidwa paku khulupirira izi “Pakuti ucimo, Pamene unapeza cifukwa lamulo, unandinyenga ine ndi kundipha nalo.” **Aroma 7:11**
- ✓ Lamulo iti phunzitsa pa ucimo, osati ciyero – ci lako-lako ca ucimo kupitila mu lamulo cinabala imfa mwa ife (**Aroma 7:5**), cifukwa kopanda lamulo cimo ndi lakufa. **Aroma 7:8**
- ✓ Lamulo ndi lokufa cifukwa mphamvu za lamulo ziri mthupi. “Popeza cimene cilamulo sicinathe kucita Popeza cinafoka mwa thupi; Mulungu ana mutumiza mwana wace wa iye yeka m’cifanizo ca thupi la ucimo.” **Aroma 8:3**
- ✓ Osatira malamulo alinaco ci lako-lako cocita cilungamo koma alibe mphamvu zocita cilungamo. “Pakuti ndidziwa kuti mkati mwanga, ndiko mthupi langa, simukhala ncinthu ca bwino – pakuti kufuna ndiri nako koma kucita ca bwino sindicipeza.” **Aroma 7:18**

2. ‘Ndi khulupirira mu cisomo, koma ndi funikanso lamulo kuti ziyenderane.’

- ✓ Zomwe timati “ziyenderane” Mulungu azica ‘kusakaniza’
“Koma ngati kuli ndi cisomo, sikulinso ndi ncito ai, ndipo pakupanda kutero, cisomo sici nkhalanso cisomo.” **Aroma 11:6**
- ✓ Kuti cisomo cikhale ca mphamvu cikhalebe co sasithidwa – Aroma 1:16, Agal 2:21
Uthenga wa bwino wa cisomo wamene Paulo ana phunzitsa ndiye mphamvu ya Mulungu ya kupulumusa munthu **Aroma 1:16**. Ngati tibwereranso kusaitira malamulo. Tikhale Tilibe kanthu ndi Khristu. **Agalatiya 5:4**

3. ‘Cisomo ndi citupa ca cimo’

- ✓ Cisomo sici uza anthu kuti adzicimwa – “Pakuti caonekera cisomo ca Mulungu cakupulumusa anthu onse. Ndi Kuti phunzitsa ife kuti pokana cisapembezo ndi zi lako-lako za dziko lapansi, tikhale ndi moyo m’dziko lino odziletsa, ndi olungama, ndi opembedzai aku lindira ciyembekezo codala ndi maonekedwe aulemelo.” **Tito 2:11-14**

- ✓ Cisomo ndico cinthu cekha cingaticose mu cimo pakuti ucimo udza cita ufumu pa inu Popeza simuli a lamulo koma a cisomo.” **Aroma 6:14**
- 4. ‘Ndi khulupirira mu cisomo, koma Tifunika kucita mbali yathu’**
- ✓ Mbali yathu ndi kukhulupirira kuti adacita zonse. “Yesu anayankha nati kwa iwo, ncito ya Mulungu ndi iyi, kuti mu khulupirire iye amene iyeyo anamthuma.” **Yohane 6:29**
 - ✓ Olungamisidwaakhalira mu cikhulupiriro – “Ndina pacikidwa ndi Khristu: koma ndiri ndi moyo wosatinsine ai, koma Khristu ali ndi moyo mwa ine. Koma moyo umene ndiri nao tsopano mthupi, ndiri nao mu cikhulupiriro ca mwana wa Mulungu amene andikona nadzipereka yekha cifukwa ca ine.” **Agalatiya 20:20**
- 5. ‘Ngati ufuna dalitso la Mulungu, pali mtengo wopereka’**
- ✓ Tina dalisidwa ndi zinthu zonse. “Wolemekezeka Mulungu ndi atateambuye wanthu Yesu Khristu amene anati dalitsa ife ndi dalitso lonse la mzimu m’zakumwamba mwa Khristu.” (**Aefeso 1:3**). Koma muthange mwafuna ufumu Wace ndi cilungamo cace, ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwa inu.” **Mateyu 6:33**
 - ✓ Mtengo udapelekedwa khale wokwanira zonse zinthu tina patsidwa mwaulele cifukwa ca Yesu Khristu. “Iye wamene sanatimana mwana wace wa iye yekha koma anamphereka cifukwa ca ife tonse, adzalekelanji kutipatsanso ise zinthu zonse kwaulele Pamodzi ndi iye” **Aroma 8:32**
- 6. ‘Ndi cisomo palibe zoti patsa, tumikira ndi mvera’**
- ✓ Cisomo cimaesera poyera anzeli zonyenga mu umoyo wa ci Khristu
 - ✓ Koma sici matilengesa kukhala ofoka. Cisomo ci ma tipatsa mphamvu zo tumikira mulungu kupambana ndi mwamene tinga kwanilisire mwa mphamvu zathu. “Koma ndi cisomo ca Mulungu ndiri ine amene ndiri, ndipo cisomo cace cakwa ine sicinakhala copanda pace, koma ndina gwirira ncitoya kuculuka yaiwo onse; si ine, koma cisomo ca Mulungu ca kukhala ndi ine.” **1 Akorinto 15:10**

Zokambirana

1. Kambiranani tanthauzo la ‘zobvomerredzedwa’ ndi ‘cisomo’ zapatsidwa mu phunziro iyi.
2. Kodi ndi yoti malamulo yopangidwa ndi anthu yomwe mundagwirilila khale yomwe yadakubweretsani pau lamulirowa zobvomerredzedwa cabe?
3. Anthu okokha zobvomerredzedwa ndi anthu acilungamo. Amafuna kukondweretsa Mulungu ndipo akhulupirira kuti njira yomwe akonkha ndi yoonadi. Koma zobvomerredzedwa ziwapeleka ku ncito za kufa ndipo amagonja. Kodi mkhalidwe wathu ufunika kukhala wotani kulingana ndi anthu okonkha zobvomerredzedwa?
4. Kodi mkhalidwe wokonkha zobvomerredzedwa ndi woopedza bwanji ku umoyo wathu wa ci Khristu?
5. Cofunikira kwambiri kukana ku ciphunzitsa ca cisomo ndi cakuti sindiye ndanga yocitira ucimo. Kodi ungatsutse bwanji kalankhulidwe aka?
6. Kodi ci Khristu cofuna malipiro ndi cotani? Ndipo cisomo citi masula bwanji?
7. Kodi cisomo ca kupanga waulesi mkukhala ndi kutumikira Khristu?

6) CIKHULUPIRIRO

“Pakuti uthenga wabwino sundicititsa manyazi, pakuti muli mphamvu ya Mulungu yaku phulumutsa munthu ali yense wakhulupirira; kuyambira m’yuda, ndiponso mhelene. Pakuti m’menemo caonetsedwa cilungamo ca Mulungu ca kucokera kuci khulupiriro kuloza kuci khulupiriro: monga kwalembedwa, koma munthu wolungama adzakhala ndi moyo ndi cikhulupiriro.” **Aroma 1:16-17**

Uthenga uonesera cilungamo cocokera kuci khulupiriro kufika kuci khulupiriro. Ciphunzitso conse cocokera kuci khulupiriro kufika ku ncito ndi uthenga wabodza. ‘Olungamisidwa adzakhala mucu khulupiriro’.

1. Cikhulupiriro cimayanjana ndi cisomo

- ✓ Zotulukamo Pomwe munthu adali pansu pa lamulo inali ncito, ise zotulukamo pansu pa cisomo ndi cikhulupiriro. **Yohane 6:29**
- ✓ Cisomo ndi Zomwe Mulungu aticitira; cikhulupiriro ndi momwe tilandira Zomwe aticitira.
- ✓ Cikhulupiriro ndi kuyankha kwathu kuzimene Mulungu adatipasa mwa Khristu.
- ✓ ‘Adatisegulira njira paku khulupirira tilowemo mu cisomo comwe tiimirapo.’ **Aroma 5:2**
- ✓ Cikhulupiriro sicitipulumusa. Yesu ati phulumutsa; cikhulupiriro cilengetsa kuti timugwiriritse iye.
- ✓ Tindapulumusidwa mu cisomo, kupyolera mucu khulupiriro, koma ngakhale cisomo ndi mpatso yocoka kwaMulungu.
- ✓ Momwe tidalandirira Yesu kupyolera mucu khulupiriro, momwe tikhale mucu khulupiriro.
- ✓ Paulo anakhalipila aku Galatiya cifukwa anawanyengelela kuwa cosa mu cikhulupiriro ndi kuwa pereka ku ncito za thupi kuti apeze cilungamo. “Adawa funsa; kodi muli opusa otere? Popeza mudayamba ndi mzimu, kodi tsopano mutsiriza ndi thupi?” **Agalatiya 3:3**
- ✓ Popanda cikhulupiriro cosatheka kumukondweretsa iye. Zonse palibe cikhulupiriro ndi za ucimo.

2. Khrist ndiye wolanganapo wofunikira pa cikhulupiriro cathu

- ✓ Anthu ayesa kukhala mwacikhulupiriro mu cikhulupiriro. Koma cikhulupiriro cifunika kukhala ndi coonerapo.
- ✓ Cikhulupiriro si nkhani koma cimene ukhulupiriramo.
- ✓ Mphamvu za cikhulupiriro cathu icokera ku cinthu cimene tikhulupiriramo.
- ✓ Ndipo cinthu cofunikira ca cikhulupiriro cathu ndi Khristu.
- ✓ Cipangano conse cakhale, kufika ngati 80% ya buku lopatulika, cikhulupiriro cindakambidwapo kali 15. Yankho ndiya kuti oonerapo ofunikirawa cikhulupiriro ndi Yesu Khristu, adali asanabwera, “Komatu lembo unasekereza zonse pansu pa ucimo kuti lonjezo la cikhulupiriro ca Yesu Khristu lika patsidwa kwa okhulupirirawo, koma sicinadze cikhulupiriro tina sungidwa po mvera lamulo otsekedwa kufikira ku cikhulupiriro cimene cika bvumbulisidwa bwino-bwino.” **Agalatiya 3:22-23**
- ✓ Ndime 115 zili mu cipangano catsopano zi phunzitisa kuti munthu akakhulupirira mwa Khristu (mau ocita) iwo aphulumusidwa, alinawo umoyo wamuyayaya, alungamisidwa, ndi zina zotero. Moikilapo ndime 35 zilankhala kuti aphulumusidwa, alungamisidwa, kapena akhala olungama mwa cikhulupiriro (liu). Zonse=kali 150.
- ✓ Mdime zonsezi palibe zofunikira zoikidwapo. Palibe zosakanizidwa kapena kuonjezedwapo ku cikhulupiriro kuti zikwanisire cipulumutso.
- ✓ Cikhulupiriro cathu sicili mubaibolo, koma mwa Khristu. Baibolo ibvumbulutsa za Mulungu. Tingadziwe Baibolo koma osadziwa Khristu, momwe adacitira Afarisi, (**Yohane 5:39-40**). Adakamvetsetsa Baibolo adakamudziwa iye, **Yohane 5:46-47**.
- ✓ Tinga ziwise buku lo patulika koma osadziwa Yesu. Monga mwamene analili Afarisi “musa thuta mu malembo Popeza muyesa kuti momwemo muli nao umoyo wo satha, ndipo akundicitira ine umboni ndi iwo omwewo, ndipo simufuna kudza kwaine, kuti mukhale nao umoyo.” **Yohane 5:39-40**
Afarisi ngati adamvetsetsa buku lo patulika bwino-bwino ngati anamuziwa Yesu.
- ✓ Cikhulupiriro coonadi ciona kwa Khristu. Khusulako zoti ndikhulupirira pa iye nthawi zonse.
- ✓ ali naco cikhulupiriro amupanga kukhala wa mtengo wapatali Yesu ‘...kuli inu okhulupirira ndi wa mtengo wapatali...’ (**1 Petro 2:7**).
- ✓ Kukulukisa cikhulupiriro mwa Mulungu kufunika nzeru zomziwa iye, Zoonapo ndi cikhulupiriro cathu.

3. Mayamiko ndiye cilakhulo ca cikhulupiriro

- ✓ Kung'nguza ndi kudandaula ndiye cilankhulo ca kusa khulupirira.
- ✓ Kuyamika ndiye cilankhulo ca cikhulupiriro. Tiyamika Mulungu pa ncito yimene anagwira mwa Yesu Khristu.
- ✓ Ndipo mwa iye tipitiridza kupereka nsembe zamayamiko kwa Mulungu, ndiye zipatso zam'kamwa mwathu, kupereka Mayamiko kwa dzina lakhe' (Aheb. 13:15).
- ✓ Yesu adaonetsera cikhulupiriro cake kwa Atate ake pa kupereka Mayamiko.
- ✓ Pakudyesa mazama yasanu anthu ndi m'khate ndi nsomba(**Yohane 6:11**) mabwato ena anabwera kucokera ku Tiberi - **Yohane 6:23**
- ✓ Ndi pakuutsa Lazaro "Yesu anayamika kwa Atate ace pakumumvera" **Yohane 11:41**
- ✓ Mwaici Yesu ana pereka umboni kuti atate ali ndi mphamvu pa zonse.
- ✓ Timaonetsa cikhulupiriro munjira imodzi-imodzi , 'm'zonse Perekani mayamiko'(**1 Athes. 5:18**)
- ✓ Osati cabe zomwe aticitira koma palizomwe azacitanso.
- ✓ Anati panga kukwaniritsa zinthu zonse. Mulungu adatipatsa cipulumutso mwa Khristu, wapangaso njira yopezeramo zonse tingafune kwa iye. **Aroma 8:32**
- ✓ 'Kuzikidwa ndi kumangidwa mwa iye ndi kukhazikisidwa mu cikhulupiriro, ngati momwe mudaphunzitsiridwa, kukahalebe mwa ico ndi mayamiko.' (**Akol. 2:6 ndi 7**)
- ✓ Mwa ici, tipereke 'maphempe ndi mayamiko' Afili. 4:6; ndi 'kupitiriza mofunitsitsa mu phempero, kupenyetsetsa kuti zonse ndi ciyamiko'(**Akol. 4:2**).

Zokambirana

1. Kodi ndi cifukwa ciani cilungamo ca Mulungu, monga cinabvumbulisidwa muuthega, 'ci coka ku cikhulupiriro kufika ku cikhulupiriro'?
2. Kambiranani momwe cikhulupiriro ndi bwenzi ndi cisomo.
3. Kodi ndi cifukwa ciani cikhulupiriro cindakambidwapo pang'ono mucipangano cakhale, kulinganiza ndi cipangano ca tsopano?
4. Kodi muganizirapo kuti ndi cifukwa ciani cikhulupiriro cikondweretsa Mulungu?
5. Kambiranani kuti ndi ciopsedzo cotani cokhala ndi nzeru zo dziwa Baibolo kwambiri koma sudzipereka kwa Yesu kuti ukhale ndi cikhulupiriro mwa Khristu.
6. Patsani zitsanzo Pomwe mu Baibolo,
 - a) Kudandaula kunali kuonetsera kusa khulupirira ndipo
 - b) Kuyamika cinali cilankhulo ca cikhulupiriro
7. Patsani citsanzo mwa izi kucokera ku umoyo wanu.

7) CIPANGANO CATSOPANO

Werengani Agalatiya 3:5-9. Mulungu ndi Mulungu wa cipangano. Kuti tigwirizane ndi iye tifunikira kumvetsetsa cipangano.

- ✓ Lonjezo la cipangano lomwe Mulungu adapangana ndi Abrahamu ndilo funikira, cipangano cacikulu mu Baibulo.
- ✓ Cinena pa ndondomeko ya Mulungu yakuombola dziko lonse, ndipo ndi cimodzi-modzi ndi cipangano ca cisomo, **(3:8)**
- ✓ Muzipangano zonse cilungamo cipatsidwa kwa iwo okhulupirira Khristu.

Tsono n'cifukwa ciani cipangano ca Mose n'cofunikira? Ndipo pali lonjezo bwanji ndi cipangano ca lonjezo? Mu Agalatiya 3 Paulo anena ndondomeko zinai:-

1) Cipangano ca lonjezo ndi Abrahamu sicidasulidwe, kusintha zina, kapena kuikapo lamulo pa ico, (Agal 3:15-17)

- ✓ 3:15. Zitakazikitsidwa, cipangano cilibe zo satilapo sicinga sinthidwe kapena ku gwedezedwa ndi mkhalidwe wa munthu.
- ✓ Mulungu yekha Adaimirira pa cipangano ca lonjezo ndi Abrahamu, (Ahebri 6:13-18). Ndi cipangano cimene sicinga gwedezedwe
- ✓ 3:16. Ma lonjezo adapangidwa kwa Abrahamu ndi Khristu. Tipindula cifukwa tili mwa Khristu.
- ✓ 3:17. Lamulo idabwera patapita zaka 430 pomwe cipangano ca lonjezo citacitika. Ngakhale idali lotani lingo lake, ico, munjira iliyonse, sicidasulise cipangano ca Mulungu ndi Abrahamu.

2) Lamulo sidapatsidwe kuti njira ina yaci khulupiriro yoti tinga pulumukilemo (Agal 3:18)

- ✓ 3:18. Mulungu sadapulmutse Abrahamu kupyolera mu lamulo koma kupyolera mu ci khulupiriro mu mbeu ya Mulungu yomwe idali kudza.
- ✓ Ngati cilungamo cidabwera kupyolera mu lamulo, Mulungu sadakatuma mwana wace kuzatifera “pakuti cidapatsidwa cilamulo cakukhoza kucitira moyo, cilungamo cikadacokera ndithu ku lamulo?” **Agalatiya 3:21**

3) Lingo la lamulo lidali kulimbikitsa cipangano ca lonjezo (3:19-25)

- ✓ 3:19a. ngati lamulo sindapatse cilungamo ndiponso sitipatula ise, n'cifukwa ciani idapasidwa?
- ✓ Idapasidwa cifukwa 'ca kulakwa', mwa citsanzo Aisraeli ankhayamba kupembeza mafano. Lamulo linawa lengesa kukhala opatulidwa na Mulungu.
- ✓ Pomwe Mulungu adatulusa Aisraeli mu Igupto, adapanga cipangano nawo cowasogolera ngati mitundu, potukuka, m'cikhondwerero ndi muma khalidwe. Ndiyo njira imodzi idali yowasungilamo ngati anthu opatulika omwe adaitanidwa kusunga lonjezo lakubwera kwa mbeu ija. “Ada sungidwa pansu pa lamulo” **(3:23)**
- ✓ 3:21-22. Lamulo simudaniwa lonjezo. Idatumikira ndi kulimbikitsa lonjezo.
- ✓ Yanali ma konzedwe apadera, yoikidwapo zosakhalapo; osati cipangano copitirira, ngati momwe ena amanenera **(3:19 ndi 25)**.

4) Lamulo ikatamangila pa tembelero; Lonjezo iwonesedwa ndi dalitso (3:10-14)

Kusiyansa ndi 3:19 ndi 10. Pansi pa cipangano catsopano.

Tili omasuka ku tembelero cifukwa Khristu adakhala tembelero; mwa citsanzo 'otembeleredwaiye' kwa ise.

- ✓ Tembelero ili idaonesedwa ndi momwe adafera Khristu. “Pakuti wo pacikidwa pa mtengo atembeleredwa ndi Mulungu” **Deuteronomo 21:23**
- ✓ Adabvutika ndi tembelero la lamulo kufikira, 'anathi kwathaa', moonjezerapo kufikira zitakwanirisika lamulo ndi tembelero.
- ✓ Njira yomwe tingafike po tembeleredwa ndi pakufuna kukhala pansu pa lamulo.
- ✓ 3:13-14. Sitili otembeleredwa, koma odalisidwa, **(onani 3:8, 9, 14)**.
- ✓ Tifunika kuwerenga ma dalitso, osati ma tembelero! Mwa citsanzo. Aef **1:13-14; 1 Akor. 2:9-12**.

Cipangano cakhale ndi cipangano catsopano cidakambidwa bwino pa nkhani ya Sara ndi Haga, (Agal. 4:21-31).

- ✓ Ayuda adazikwedza kuti adali ana a Abrahamu, koma adali ana awiri kwa azimai osiyana. Umunthu wa mwana unali kuonesedwa ndi momwe adali amai awo. “Ndi uzeni inu akufuna kukhala omverera ma lamulo. Kodi simukumva cilamulo? Abrahamu adali nawo ana amuna awiri, umodzi obadwa mwa m’dakazi, umozi mwa m’fulu **(Agalatiya 4:21-22)**.
- ✓ Izi zidaimilila zipangano ziwiri za lonjezo (Sarah) ndi lamulo (Hagara).
“Pakuti akaziwa ali ma pangano awiri, m’modzi waku Phiri la Sinai, akabalira ukapolo, ndiye Hagara. Koma Hagara ndiye Phiri la Sinai mu Arabiya, na fanana ndi Yerusalemu wa tsopano pakuti ali muukapolo Pamodzi ndi ana ace. Koma Yerusalemu wakumwamba uli waufulu ndiwo amai wathu.” **(Agalatiya 4:24-26)**
- ✓ Paulo anati “Koma ife, abale, monga Isake tili ana a lonjezani” **(Agalatiya 4:28)**
- ✓ Adafunsa aci lamulo kuti mai wanu ndi Ndani?
- ✓ Agal. 4:30. Lamulo ndi cisomo sizinga khale Pamodzi. Cimodzi cifunika kupita. Pomwe Ishaele adacotsedwa, mtendere udabwera m’nyumba ya Abrahamu. Ndi pokhapo tikacoka ku zololedwa cabe ndi pomwe tiza ziwa mtendere.
“Koma lembo linena ciani? Taya kubwalo m’dakazi ndi mwana wace, pakuti sadzalowa nyumba mwana wa m’dakazi Pamodzi ndi mwana wa m’fulu.” **Agalatiya 4:30**
- ✓ Osasakaniza zipangano. Osaika cigamba catsopano pa cobvala cakhale. Tayani cobvala cakhale. Bvalani ca tsopano.
- ✓ Agal. 5:1. Tifunika kumenyana nayo nkondo yonse yofuna kutipereka ku ukapolo wa lamulo....”Cirimikani musakhondwenso ndi gori la lamulo” **Agalatiya 5:1**

Zokambirana

1. Kodi kulingana kwake ndi kusiyana kwake ndi kotani pa cipangano ca ci lonjezo, comwe Mulungu adapanga ndi Abrahamu, ndi cipangano catsopano comwe ife tilimo?
2. Kodi cipangano ca Mose ndi copambana kapena ndi cosapambana ku cipangano ca ci lonjezo? Cifukwa?
3. Monga mwa Agalatiya 3:21 ndi Aroma 10:3 kodi ndikusokoneza kwa bwanji komwe a Yuda adacita?
4. Kodi ndi njira yotani yomwe cipangano ca Mose cidathandiza cipangano ca ci lonjezo?
5. Kodi mudamverelapo kuci phunzitsa cabodza ca ma tembelero? Kodi zopitamo zinali zotani?
6. Lembani ma dalitso yomwe yali yathu mwa Yesu Khristu.
7. Kodi mudathengapo thapulo ‘yocotsa m’dakazi wa ukapolo’ pa umoyo, mwa citsanzo kutaya ma buku, ma CD, ma DVD yomwe yanali kuphunzitsa zobvomerzedwa kapena zosakaniza? Kodi mudazipatulapo ku anthu omwe maphunzitsa awo adali nayo mphamvu yo kubweretsani mu ukapolo?
8. Kodi ndi njira yotani yomwe mudamenyerapo nkondo yofuna kukubwezerani mu ukapolokwa lamulo?

8) ANA A MULUNGU

- ✓ Panthawi ya cipangano cakale anthu a Mulungu adali kukhala pansi pa ulamuliro wa lamulo. Izi zionetsedwa ndi mwambo wa mwana okhala pansi pa m'phunzitsi (kapolo wa m'nyumba) m'nthawi ya cipangano catsopano. "Lamulo inali m'phunzitsi wathu wotileta kuli Khristu kuti tiphulumusidwe kupyolera mu cikhulupiriro." **Agalatiya 3:23-24**
- ✓ Panthawi yomweyi 'mwana' sadali kusiyana ndi kapolo wa m'nyumba. "Pokhala wolowa m'nyumba ali wa khanda sasiyana na kapolo angakhale ali mwini zonse, kufikira nthawi yoikika khale ndi atate wace." **Agalatiya 4:1-2**
- ✓ Koma panali nthawi imodzi, yomwe idali yapadera, pomwe izi zinkasinthidwa. Ndipo mwana adali kutengedwa kukhala mubanja ya atate ace. Sadali 'mwana wacicepere' koma mwana 'wofikapo'.
- ✓ Mtanda ndiwo udasinthisa pomwe anthu a Mulungu sadaliso acicepere koma anali wofikapo. "Koma pokwaniridwa nthawi, Mulungu anatuma mwana wace wobadwa m'dakazi wobadwa wakumvera lamulo kuti akaombole iwo akumvera lamulo kuti ife tikhalandile umwana." **Agalatiya 4:4-5**
- ✓ Izi zidaoneseredwa ndi:-
 1. Kumasulidwa ku m'phunzitsi (lamulo. "Popeza cadza cikhulupiriro sitikhalanso omvera namkungwi" **Agalatiya 3:25**
 2. Kugwirizana bwino ndi atate. "Ndinu ana a Mulungu kupyolera mu cikhulupiriro mwa Yesu." **Agalatiya 3:26**
- ✓ Yesu adati, 'kapolo sakhalirira m'nyumba, koma akhalirira muyaya; (**Yoh. 8:35**). Kapolo atumikira kuti asunge malo ace m'nyumba, malo a mwana m'nyumba ndi ake cifukwa sikuti atumikira koma cifukwa cakuti ndiye gawo lake ngati mwana.

Tindamwalira ku lamulo ndipo ndise amoyo ku M'zimu

- ✓ Kwa okhulupirira M'zimu Woyera adatenga malo a lamulo. "Ngati M'zimu akutsogolerani simuli omvera lamulo" **Agalatiya 5:18**. Tina mwalira ku lamulo, tili amoyo ku M'zimu.
- ✓ Mu **Agal. 4:4** tiwerenga kuti Mulungu adatuma mwana wace; mu **Agal. 4:6** tiuzidwa adatuma M'zimu wa mwana wace.
- ✓ Mwa Khrist tili nayo malo a mwana; kupyolera mu M'zimu timamvera ubwino wa umwana. M'zimu atithandiza kuti timvera ngati ana ndi kugwirizana ndi Atate ngati adacitira Yesu Khristu.
- ✓ Sicofunika kutiwo adzalandira m'khalidwe wa umwana akhale ogwirizana ndi Atate kupyolera mu lamulo, ndondomeko, zololedwa, ndi zina zotero. Uku kungakhale kubwerera ku m'khalidwe waumwana waci cepere, kapena ukapolo.
- ✓ Mwa cisoni ici ndico Agalatiya anacita Pamene anabwereranso ku malamulo. "Mubwereranso bwanji mukusata miyambo yofoka ndi yaumphawi, imene musunga Masiku ndi miyezi imene mufuna kubwerezanso kuicitera ukapolo? musunga masiku, ndi miyezi, ndi nyengo, ndi zaka .ndiopera inu, kuti kapena ndadzibvutitsa ndi ina cabe." **Agalatiya 4:9-11**

M'khalidwe wa mwana wuonesedwa pa kumvera bwino ndi Atate.

- ✓ Maganizo a 'kapolo' aonesedwa ndi malamulo ndi opatsa malamuluwo. Anthu ali ndi maganizo a ukapolo nthawi zonse ayembekeza kuuzidwe zoti acite.
- ✓ M'khalidwe wa mwana wofikapo wuonesedwa pa kumverana bwino ndi Atate.
- ✓ Ana atsogoreledwa ndi M'zimu. "Ambiri omwe atsogoreledwa ndi M'zimu wa Mulungu, awa ndi ana a Mulungu" (**Aroma 8:14**).
- ✓ Pansi pa cipangano catsopano pali mbali ya pamwambaina yakumverana bwino yoonosedwa ndi ubwenzi watsopano. Palibe okhala pakati pa ise ndi Mulungu. "Palibe azaphunzitsa bwenzi lake, kapena mbale wake, Kunena, "DZIWA AMBUYE", Popeza onse azandiziwa, kuyambira wamng'ono kufikira wamkulu" (**Aheb. 8:11**).
- ✓ Pomwe sumvetsetsa kutindiwe mwana ndi pomwe uzakhala ndi m'khalidwe wa ukapolo. Udzafunika ndondomeko ndipo wina akuuze zocita.
- ✓ Yesu adati, 'Khosa zanga zimvera liu langa'. Tiphunzira kuziwa liu lake, ndi kuli siyanitsa ndi liu la ena a cilwendo.

- ✓ Dziwa m'khalidwe wake ndiponso udzadziwa liu lake.

Zokambirana

1. Kodi ndi cifukwa ciani mtanda udali kuoneretsa kuti sinditse akapolo koma ana? Kodi ndi kusintha kuti kwina kudacitika pa mtanda kwa anthu a Mulungu?
2. Kodi ndi cifukwa ciani n'cofunikira kumasulidwa ku lamulo kuti timve bwino kuyanjana ndi Atate?
3. M'zimu Woyera atenga malo ya lamulo mu umoyo wa okhulupirira. Kambiranani ncito ya M'zimu Woyera mu umoyo wa Mkhristu.
4. Ndiye ncito yake Satana yokhazika anthu a Mulungu pansi pa lamulo, kapena kubweretsa omasuka pansi pa lamulo. N'cifukwa ciani ziri motero?
5. Kukhala omasuka pakufuna kuti munthu akhale pakati pa Mulungu si kutanthauza kuti kulibe malo ya a zibusa, aphunzitse, atsogoleri ndi ena otere mu mpingo. Kodi mungalankhule bwanji kusiyana kwa kamveredwe ka zinthu za Mulungu paka kucetekera wina, ndi paku pezerapo zabwino kupyolera mu azibusa, aphunzitse ndi ena otere?
6. Kodi muma dzindikira bwanji liu la M'zimu Woyera mu umoyo wanu? Kodi mungadziwe bwanji monga mwa mamveredwe anu?
7. Gawani kamvekedwe ka kukula ndi kuyenda patsogolo kwa kuyanjana ndi Atate

9) MBADWO WATSOPANO

Baibulo imalankhula pa cilengedwe cathu pawiri:

1) Cibatwa cathu cakale, comwe tinkakhala naco comwe tinalandira kucoka kwa Adamu titango mbadwa cabe. “Ndipo inu akupatsani moyo pokhala munali akufa ndi zolakwa, ndi zocimwa zanu, zimene munayendamo kale, monga mwa mayendedwe a dziko lapansi lino...” (**Aefeso 2:1-3**)

2) Cibatwa catsopano cathu comwe tinalandira paku badwanso tsopano. Tina batiziwa mwa Khristu, ndipo ‘titengako mbali ku Cibatwa ca Mulungu’, (**2 Pet. 1:4**). ‘Cono ngati munthuali mwa Khristu, niolengedwa kwatsopano; zakale zapita, zimene zilipo ndi za tsopano’, (**2 Akor. 5:17**).

Izi zitanthauza

- ✓ Tina mwalira kucoka momwe tinaliri mwa Adamu ndise ogwirizana ndi Khristu. ‘Iye amazipereka kwa Ambuye, iyeyo ndi Ambuye amakhala mzimu umodzi’ (**1 Akor. 6:17**)
- ✓ Ngati nthambi imaikidwa bwino ku mpesa, naisenso timaikidwa kuli Khristu ali moyo wathu...’ (**Akolose. 3:4**).
- ✓ Cipangano cakhale cinkapatsa malamulo, cipangano catsopano nico patsa umoyo.
- ✓ Tinali mtundu wina wa cilengedwe koma tsopano ndise ena. Tinali akufa koma tsopano tili ndi umoyo. Tinali mumdimba koma tsopano tili mkuwala. (**Onani Aefeso 2:1, 5:8**)
- ✓ Komadi mbadwo watsopano sungacimwe ndipo sufuna ngakhale kucimwa! “Tiana, munthu asasokeretse inu iye wakucita colungama ali wolungama, monga iye ali wolungama...yense wobadwa kucokera mwa Mulungu sacita cimo, cifukwa mbeu yace ikhala mwa iye ndipo sakhoza kucimwa, popeza wobadwa kucokera mwa Mulungu” (**1 Yohane 3:7-9**)

Koma a Khristu acimwabe

Kodi muma cita ciani muka cimwa? Pomwe Mkhristu acimwa, zinthu ziwiri zifunika kumvetsetsa kadziwikidwe ndi mkhalidwe wathu.

- ✓ Kudziwika kwathu kuli mwa Khristu; ndi momwe tiliri mwa iye. Ndi momwe tiliri mu mzimu wathu.
- ✓ Wolemba Ahebri akamba za ise kuti ‘mizimu ya olungama amene Mulungu wawasandutsa angwiwo kweni-kweni’ (**Aheb. 12:23**).
- ✓ Mwa iye tili angwiwo, opanda cimo ndipo osonongeka. Mzimu wathu sungaonongeka ndi cimo.
- ✓ Mkhalidwewathu umacitikira mthupi, mu Umunthu wathu. Macitidwe a ucimo akhala mthupi yathu yosaomboledwa. Tingayesedwe, ndipo zimaticikira. Tinga cimwe, ndipo nthawi ina tima cimwadi.
- ✓ Izi zikacitika mzimu wathu umazonnda zotere. Cifukwa Tilibe Cibatwa ca ucimo. Tili naco cilengedwe copatulikandipo izi zitsutsana ndi cimo. “Koma ngati ndi cita cimene sindifuna sindineno amene ndi cita, koma ucimo wa kukhala mkati mwanga ndiwo. Ine ndi kondwela ndi cilamulo ca Mulungu, koma ndiona lamulo lina m’ziwalo zanga, lili kulimbana ndi lamulo la mtima wanga.” (**Aroma 7:20, 22-23**).
- ✓ Ndipongatimkhristuacimwa ,nkhondoimacitikamwaiye.thupikuukiramzimukapenamzimukuukirathupi.

Penya mu galasikudziwa coonadi pa iwe!

- ✓ Pakati pa nkondo imeneyi Satana amayetsesa kuti tiziwike ndi mkhalidwe wathu.
- ✓ Tifuna kudziwa pa kusiyana pakati pa mkhalidwe womwe umacita mthupi ndi kudziwika kwathu kuti ndise yani mu Mzimu. “Ngati Khristu ali mwa inu, thupi lidafa cifukwa ca cimo, koma Mzimu ndi umoyo cifukwa ca cilungamo” (**Aroma 8:10**)
- ✓ Mtsokonezo sunga khalepo paku Penya ku mau a Mulungu osati ku mkhalidwe wathu.
- ✓ Mulungu abvumbulutsa coonadi ca ise kukhala ngati mbadwo watsopano. Monga galasi ibvumbulutsa nkope latu.
- ✓ “Paja munthu amene amagomva cabe mau, osa cita zimene mamvazo, ali ngati munthu wo yangana nkope yace yacibatwa mu galasi, Tsono amati akazipenya, amacokapo, posacedwa nkuiwala m’mene aonekera” (**Yak 1:23-24**)
- ✓ Yakobo anena pa munthu yemwe abvutika kukhala momwe afunikira cifukwa azi iwara momwe aliri.
- ✓ Mkhalidwe suti londola ise. Zomwe Yesu adacita ndiye zomwe zitilondola.

- ✓ Pomwe timaona m'galasi la mau a Mulungu ulemerele wa momwe tiliri mwa Khristu ngakhale mkhalidwe wathu usinthidwa mu maonekedwe amenewo.
- ✓ Coonadi ciri mwa isemwa mzimu wathu ndipo cioneretsa cekha mwa mkhalidwe wathu, "Tonsefe opanda copimba nkhope yathu, Timaonetsa ulemerele wa Ambuye, ngati momwe galasi lima onesera nkhope ya munthu. Monsemo Ambuye athu amene ali mzimu, amatisandutsa kuti tifanane naye, ndi kukhalanawo ulemerele wake muculukira-culukira, ngati mwa mzimu wa Ambuye" **(2 Akor 3:18)**.
- ✓ Sitingakhale momwe tiliri kufikira titadzidziwa.

Zokambirana

1. Pa cipulumutso tidamwalira komwe tinaliri, Pamodzi ndi mbadwo wakhale. Tidabadwatso mwa tsopano pakutengako mbali ku mbadwo wapadera. Ena amaphunzitsa kuti tiri ndi mbadwo ziwiri; mbadwo wakhale ndi watsopano. Maganizo anu ni otani pa izi? Muganiza tili ndi mbadwa iwiri, kapena cabe mbadwo watsopano?
2. Tikalibe kufika pa muthu uyu munamvera bwanji pomwe Yohane adanena kuti Akhristu samacita ucimo ndipo sungacimwe (1 Yohane 3:7 ndi 9).
3. Kodi muma cita ciani ngati mwa cimwa?
4. Kambiranani zomwe mumvetsa pa kusiyana kwa mkhalidwe ndi kudziwika.
5. Kale, kodi mumalangana kuti pofuna kuzi dziwa mkhalidwe kapena momwe tizionera mu Mulungu?
6. Kodi mungawauze bwanji anthu amene akamba kuti maphunzitso awa alimbikitsa kuti asalangane pa mkhalidwe wao ndipo acimwe kwambiri?
7. Kambiranani mau awa: munthu azapeza kukhala kuti ndi kobvuta ngati aiwala kuti iye ndi Ndani.

10) MUNTHU WATSOPANO

- ✓ Paulo adalimbikitsa Aefeso kuti ‘...ayende moyenera ndi kuitanidwako’ (**Aefeso 4:1**).
- ✓ Kwa Afilipi adawalemba, ‘...mkhalidwe wanu ukhale oyenerana ndi uthenga waKhristu’ (**Afilipi 1:27**).
- ✓ Liu loti ‘kuyenera’ litanthauza kuti njira yeni-yeni.

Kuli njira yocitika yoonetsera cisomo ca Mulungu mu umoyo wathu tsiku ndi tsiku. Mwa cisoni, pali ziphunzitso zabodza Kunena pa izi.

Mwa citsanzo:

- ✓ Ena aphunzitsa kuperewera, mwa citsanzo, cifukwa cakeena abvutika mu Ukhristu wao nicifukwa cakuti Mulungu sanawasiye ndi zosewezetsa zokwanira. Afunikira zambiri! Izi zibweretsa mtsokonezo mthupi la Khristu pakati pa ‘zomwe ndili nazo ndi zomwe ndiliba’ ndipo zionesa kusa fikapo pa zapa uzimu.
- ✓ Ena aphunzitsa zobvomerzedwa, mwa citsanzo, Ciyero cikwanirisidwa ngati taya kapena cibwera ndi cifukwa ca ncito zathu. Cilungamo cicokera mkati mwathu cifukwa tili naco khale.
- ✓ Ena aphunzitsa kulekerera, mwa citsanzo, ‘zileke zipite ndipo leka Mulungu’. Iwo ophunzitsa kuti ciphunzitso cokweza kapena kuuza pa za makhalidwe ndi zobvomerzedwa. Paulo anali ku limbikitsa anthu cifukwa ana dziwa kuti tili nazo kale mphamvu zokhala ngati oyera.

Kodi Paulo adaphunzitsanji? Maphunzitso a Paulo ali mbali ziwiri zo patulika: Ciphunzitso ndi kukweza. Izi ziri ngati momwe irili sizara yogeleda kuwiri.

1. Kogelela koyamba: Ciphunzitso

- ✓ A) Zomwe Khristu adati citira, mwa citsanzo, adatilungamitsa, kuti fikizapo, kuti yeretsa, kukhalisa ana a Mulungu, ndi zina zotere. Izi zilankhula pa kuziwa kwathu mwa Khristu kupyolera mu ubatizo mu imfa yake, kuikidwa m’manda ndi kuukisidwa.
- ✓ B) Zomwe Khristu adati patsa, mwa citsanzo, Umoyo wake mwa ise. Zofunikira zonse za pa Umulungu zikhala mwa ise, **2 Pet 1:3**. Mwa ici, zimene Mulungu amapempha kwa ise adati patsa kale

2. Kogelela kwa ciwiri: Kukweza

- ✓ Tindaitanidwa kubvala Ambuye Yesu Khristu. Mwa citsanzo, kukhala momwe tiliri ndi kuonesera zomwe tili nazo.
- ✓ ‘...ngati osakhulidwa a Mulungu, oyera ndi okonedwa, muzikhala a mtima wa cifundo, okoma mtima, ozicepetsa, ofatsa, opirira...’ (**Akolose 3:12**).
- ✓ Tiseweza zomwe adasewenza kale mwa ise. “...gwirani ncito yace ya cipulumutso canu ndi mantha, ndi kutumikira. Pakuti wakucita mwainu ndiye Mulungu.” (**Afili 2:12-13**)
- ✓ Ticita izi mwa cikhulupiriro. “Umoyo umene ndiri nao tsopanomthupi ndiri nao m’cikhulupiriro mwa Mulungu” (**Agalatiya 2:20**). Umoyo waci Khristu ndi wa cikhulupiriro, (**Aroma 1**)
- ✓ Pomwe tibvala Ambuye Yesu Khristu mwa cikhulupiriro, sitipatsa mpata wakuti thupi iseweze. “Koma Bvalani Ambuye Yesu Khristu, ndipo musaganize za thupi kucita zofuna zace.” **Aroma 13:14**
- ✓ Pomwe tibvala munthu watsopano mwa Khristu, timasiya khalidwe la kale, **Aefeso 4:22-32**.
- ✓ Sitimayetsa kugonjetsa thupi, koma kuyenda mu Mzimu. “Muyende-yende ndi mzimu ndipo musa fitse cilako-lako ca thupi” **Agalatiya 5:16**
- ✓ Ngati tipereke ziwalo za mathupi anthu ku cilungamo sizingacitenso ucimo. **Aroma 6:13, 16, 19**.
- ✓ Kubverera kwathu kutheka cifukwa ca Mzimu Woyera. ‘Ngati mukhala mwa thupi muzafa, koma ngati mwa Mzimu mukupha ncito zonse za thupi, muzakhala ndi umoyo’ (**Aroma 8:13**)

Zokambirana

1. Kodi mudamvako kale mwa ziphunzitso izi zomwe zikambapo kayendedwa ka Khristu mofikapo, mwa citsanzo, kusowekela zina, zobvomeredzedwa ndi kugonjera ziri zonse? Ngati sitero, lankhulani zomwe mudapitamo.
2. Maphunzitso a Paulo ali monga sizara, cifukwa ciani coyamba cifunika kukhala ciphunzitso?
3. Kambiranani aya mau: 'zonse mufuna za Umulungu zikhala mwa inu'. Kodi mungasimikize mau awa kucokera mu Baibulo?
4. Kodi cifukwa ciani ndi cofunikira kulankhulapo kwambiri 'kubvala munthu wa tsopano' kupambana 'kucosa munthu wakhale' mu mau ena, ndi cifukwa ciani Paulo anena kuti Tifunika kuyenda mu mzimu, mumalo moti azilankhula kuti Tifunika kupewa kumverera zocita thupi?
5. Kodi ndi cikutandizilani cotani comwe mwapezamo mu phunziro iyi?

11) CIKONDI CA MULUNGU

- ✓ Si cifukwa cakuti mu khulupirira Mulungu ndiye cofunikira, koma zomwe mukhulupirira pa za iye.
- ✓ Zomwe ukhulupirira pali Mulungu zionetsera ubwenzi ndi iye
- ✓ Ngati ukhulupirira kuti Sali ku mbali yako uzamuopa mumalo mo mukhulupirira. Uzamutawa mumalo mokhala naye pafupi. Sunga khulupirire yemwe umamuopa ndi yemwe uganiza azakuononga.
- ✓ Kuopa kumabvutitsa koma cikondi cangwiro cicoso kuopa.
- ✓ Cikondi ca Mulungu ndiye maziko a cikhulupiriro.
- ✓ Palibe comwe tingacite kuti Mulungu atikonde kwambiri, ndipo palibe comwe tinga cite kuti ti pangitse Mulungu kutikonda pang'ono.
- ✓ Mulungu afuna tiziuka ndi kuganizira za cikondi cake pa ise.
- ✓ Cikondi ca Mulungu ndiye popumira pathu...ndi iye. "Yehova Mulungu wako ali pakati pako wa mphamvu wa ku phulumutsa, azakakondwera nawe ndi cimwemwe." (**Zefa 3:17**). Azatilengesa kupumula cifukwa ca cikondi cake.

Kodi timatenga kuti kowona zinthu zotere? Yesu ndiye 'cithunzi ca Mulungu osaoneka' (**Akol 1:15**). Cithunzi ca Mulungu cili conse cimene citsutsana ndi cimene tiona muli Yesu ndi cithunzi ca bodza.

Cibwenzi comwe adali naco ndi Atumwi ndi coonerapo ca ife momwe Mulungu afuna tikhali ndi iye.

- ✓ **Yohane 13:1**. Yesu adakonda Atumwi 'kufikira cimarizo' (Cigreek: teros = kufikapo pa cimarizo; kopanda malekerezo). 'Adawaonesa cikondi cake cofikapo' (NIV).
- ✓ Kodi cikondi cake cofikapo ndi cotani?
- ✓ Mtanda ndiye cikondi ca Mulungu cofikapo pa ise. Palibe cikondi copambana ici. "Palibe munthu ali naco cikondi coposa ici, pakuti munthu ataya moyo wace cifukwa ca abwenzi ace" (**Yohane 15:13**)
- ✓ Yesu adafuna aone kuti momwe anakondera Atumwi ndi mowme Atate akumwamba ankamukonderanso. "Mukadazindikira ine mukadadziwa Atate wangangnsa. Kuyambiranso pano mum'zindikira iye ndipo mwa muona iye. Filipo? Iye amene andiona ine waona Atate" (**Yohane 14:7-9**)

Kodi Atumwi adaziwa civumbulitso ca cikondi?

- ✓ Ena adaziwa (mwa citsanzo Yohane amene anazipatsa zina kuti ophinzira wamene Yesu anaconda.) **Yohane 13:23, onaninso Agalatiya 2:20**.
- ✓ Ena adakadziwa (mwa citsanzo Petro wamene anaganidza kuti ndiye anaconda Yesu kwambiri koma Yesu anamuonetsa kuti iye Yesu ndiye ana mukonda Petro) **Yohane 13:36-38, 21:15-17**
- ✓ Ena sadadziwiretu mwa citsanzo Yudas, ndiye umodzi cabe pa ophinzira a Yesu wamene sanaone imfa ya Yesu. (**Yohane 13:24-26**).

Yohane adzalandira civumbulitso copambana pa cikondi ndipo adali kuphunzitsa bwino. Adati phunzitsa kuti:

1. Cikondi ca Mulungu cilibe zofunikira ndiye maziko a ubwenzi ndi iye. 'Ici ndiye cikondi, osati kuti tindakonda Mulungu, koma kuti adatikonda, natuma mwana wace kuti akhale nsembe yopsereza ya macimo athu' (**1 Yohane 4:10**).
 - ✓ Tindazika mizu ndi kukhalira mu cikondi. "Kuti Khristu akhale cikhali mwa cikhulupiriro mumtima yanu, kuti ozika mizu ndi osendereka mu cikondi." **Aefeso 3:17**
 - ✓ Maria adakhala pa mapazi ace kufikira atadziwa kuti anakondedwa. Kucoka mwa izi adatamikira Yesu bwino.
2. Kudziwa cikondi ca Mulungu sikufkapo; tifikira kucikhulupiriranso. 'Tadziwa ndi kukhulupirira cikondi comwe Mulungu ali naco pa ise. Mulungu ndi cikondi, ndipo iye okhala mu cikondi akhala mwa Mulungu, ndipo Mulungu mwa iye.' (**1 Yohane 4:16**).
 - ✓ Ngati tikhulupirira cikondi ca Mulungu tima ci mvera ngakhale mkhalidwe wathu "cifukwa cikondi ca Mulungu ciratsanulidwa mu mitima mwathu mwa mzimu Woyera amene wa patsidwa kwa ife" (**Aroma 5:5**)

- ✓ Ngati si timvera cikondi ca Mulungu mkhalidwe wathu, sitizamvanso ngakhale ndi maganizo athu.
3. Cikhulupiriro cimafika pakukwima kupyolera mu civumbulitso ca cikondi ca Mulungu. 'Iye emwe acita mantha akalibe kupangidwa wangwiro mu cikondi' (1 Yohane 4:18).
- ✓ Mantha si cilengedwe ca Mulungu. Saopa kalikonse, mwa ici ciyero cake, ngati momwe aliri mu mkhalidwe wake, sadaacokere ku mantha koma ku cikondi.
 - ✓ Momwemonso, mantha sangalese ciyero mwa ise, Cikondi ndiye cikutha kutero. Kumverera cikondi ca Mulungu tizaperekedwa patali kupambana ndi momwe mantha angacitire.
 - ✓ Pomwe Mulungu akalibe kusintha, amacotsa mantha ndi kuti phunzitsa ubwino wa umoyo kupyolera mu cikondi. 'Cikondi cangwiro cicosa mantha'. (1 Yohane 4:18).
 - ✓ Palibe zobvutisitsa pa kukhala pa umoyo wauzimu ngati paku dziwa kucoka kukhala m'mantha kufikira kukhala mu cikondi.

Zokambirana

1. 'Tikhala ngati Mulungu yemwe tikhulupirira'. Patsani zitsanzo zili bwino ndi zoipa pa ici
2. Mu uthengawa Mateyu, Marko, Luka ndi Yohane, tiona momwe Mulungu aliri, pomwe tilanganira umoyo wokoma wa Yesu-Mulungu kuonekera mu munthu. Gawanani zivumbulutso zina za cikondi ca Mulungu zomwe mwalandira muuthenga unai.
3. Kodi, zoipa za bwanji zonama zomwe zinaoneretsa kuti Mulungu sindiye momwe aliri, ndipo izi zina kubvutitsa bwanji kuyanjana ndi iye?
4. Kambiranani, **1 Yohane 4:10** umu, cidaoneka cikondi ca Mulungu mwa ife, sikuti ife tindakonda Mulungu, koma kuti iye adatikonda ife ndipo anatuma mwana wace akhale ciombolo cifukwa ca macimo athu.
5. Kodi kumvera kwathu kuma cita ncito bwanji muma yendedwe athu ndi kuonetsera cikondi cathu kwa Mulungu?
6. Kodi ubvomeredza kuti cikondi ca Mulungu ciri ndi kufikapo kwakukulu kusintha umoyo wathu; ndipo kuti mantha ndiye cobvaliza cikulu kuti tisakule mukuyanjana ndi Mulungu?

12) UMOYO WOSATHA

Yesu, kupyolera mu ku khetsa mwazi wake 'adatiwombola muyaya' ise, (**Ahebri 9:12**). Ngati ana a Isreali muciphululu, Akhristu angayende nawonso muciphululu ngati asakhula kutero, koma kulibe kubwerera ku Igupto.

Tili nawo umoyo wosatha:

1) Cifukwa ca Atate

- ✓ Mdime zocepa ya Aroma, Mulungu aonetsedwa ngati woweruza. Koma adaika kuweruza konse kwa macimo athu pali mwana wake, kulingana ndi ciyero cake.
- ✓ Cifukwa ca ici sitibwereranso kuweruzidwa pa cimo. "Indetu indetu, ndi nena kwa inu iye wakumva mau anga ndi kukhulupirira iye amene anandituma ine, ali na moyo wosatha." (**Yohane 5:24**)
- ✓ Ticosedwa mu bwalo lamilandu kuperekedwa mu banja lake Mulungu. Mulungu ndiye Tate wathu. "Pakuti inu simuna landire mzimu wa ukapolo kucitanso mantha, koma munalandira mzimu wa umwana, umene tipfuula nao kuti Abba Atate. Mzimu yekha acita umboni, kuti tiri ana a Mulungu" (**Aroma 8:15-16**)
- ✓ Tifunika kumvetsetsa kuti kuphulumutsidwa kwathu sikunbwere ndi 'sankho' lakukhonka Khristu. Ifika kucoka ku muyaya kufikaku muyaya, ndi ncito ya Mulungu kucoka pa ciyambi kufika cimariziro. "Cifukwa kuti iwo amene iye anaweruzilatu iwowa anawalamuliratu afanizidwa ndi cifanizo ca Mwana Wace, kuti iye akhale mwana woyamba. Ndipo amene iye anawalamuliratu, iwo anawa itananso; ndimo iwo amene iye anawaitana, iwowa anawayetsanso olungama, nawapatsanso ulemerelo." (**Aroma 8:29-30**)
- ✓ Cipulumutso ndi ncito ya Mulungu kucokera pa ciyambi paka kumatero.
- ✓ Sitifunika kusokoneza kuganizira Mulungu alingana ndi ise. "Kodi mukazi angaiwale mwana wace wa pabele, kuli iye sangacitire cifundo mwana wobala iye? Inde awa angaiwale koma ine sindingaiwale iwe." (**Yesaya 49:15**). "Balaamu anati 'Mulungu sindiye munthu kuti aname; kapena mwana wa munthu, kuti aleke; kodi anena osacita?'" (**Numeri 23:19**).
- ✓ Tifunikira kuganizira momwe Baibulo ibvumbulutsira osati momwe anthu tiganizira. Izi zilengetsa kuti tikhale ofikapo bwino paku mvetsa.
- ✓ Onani zime Paulo anena pa ici mwa **Aroma 8:31-39**

2) Cifukwa ca Mwana

- ✓ Tindapatsidwa kwa Khristu ndi Atate kuti tisungidwe bwino. "Onse amene Atate andipatsa adzabwera kwa ine, ndipo munthu aliyense wodza kwa ine sindizamkana konse" **Yohane 6:37**.
- ✓ Tindaphimbidwa kuwiri, mwa Atate ndi Mwana '...umoyo wanu udabisidwa ndi Khristu mwa Mulungu' (**Akol. 3:3**). 'Ndiwapatsa umoyo wosatha ndipo sazaonongedwa, palibe azawacotsa m'manja anga. Atate anga amene andadipatsa, ndi wopambana onse, palibe angathe kuwalanda m'manja a Atate anga' (**Yohane 10:28-29**).
- ✓ Pomwe tindakhulupirira Yesu, tinagwirizana naye muifa, kuikidwa m'manda ndi kuukisidwa.
- ✓ Tiri ogwirizana ndi iye kukhala ziwalo zimodzi, ziwalo za Thupi Lake. "Tsono inu nonse ndinu thupi la Khristu, aliyense ndi ciwalo ca thupilo" (**1 Ako. 12:27**)
- ✓ Tiri ocingilizidwa mwa Khristu. Tika onongedwa, thupi la Khristu sikhalanso nase, ndi payekha.
- ✓ **Aroma 8:1**. Palibe m'landu wotsutsa anthu amakhala mwa Khristu Yesu. Izi zilipobe sikutanthauza kuti tsopano, osati muyaya, palibiretu zina ai!
- ✓ Ngati Mulungu adatipulumutsa tikali a ucimo, kuzapambanapo kuti sunga cifukwa tindayanjana ndi iye. Yesu ndiye moyo wathu. "Koma Mulungu asimikiza kwa ife cikondi cace ca mwini yekha m'menemu, kuti pokhala ife cikhalire Ocimwa Khristu adatifela ife. Ndipo sono popeza inayesedwa olungama, ndi mwazi wace makamaka ndithu tizapulumuka m'kwiyo wa Mulungu mwa iyeyo" (**Aroma 5:8-10**)

3) Cifukwa ca Mzimu Woyera

- ✓ Pomwe tindapululumutsidwa tinasindikidza ndi Mzimu Woyera.
- ✓ Izi zisimikiza kuti ndise ocingilizidwa kufika Yesu akatitenge kukhala ndi iye. 'Mwa iye muda khulupirira pomwe mudamva mau a coona, uthenga wa cipulumutso canu, muli iyeso, mutakhulupirira,

mudasindikizidwa ndi mzimu Woyera amene adaalonjeza, ndiye cikole kuti tizalandiradi madalitso kufikira kuombedwa kwathu, kufikira kulemekeza ulemerele wake.' (**Aefeso 1:13 ndi 14**)

- ✓ Cosindikiza ndiye coonetsera mwini wake. Mulungu adaika cosindikiza pa inu kuti aonesere kuti muli ake.
- ✓ Cosindikiza ciri ngati copereka pofuna kucita zina, ngati zoperekako, kapena mpete ya ukwati. 'Mulungu ndi wamene amatikhazikitsa Pamodzi nanu mwa Khristu. Ndiye wamene adatizodza, nasindikiza cizindikiro cake, ndi kuika Mzimu Woyeramumtima wathu ngati cikole' (**2 Akorinto 1:21-22**).
- ✓ Tindasindikizidwa kufikira tsiku loombedwa, mwa citsanzo, tsiku la kubweranso kwa Yesu Khristu, 'Ndipo musamvetse cisoni Mzimu Woyera amene Mulungu adakusindikizani cizindikiro cake cosimikiza kuti ndinu ake pa tsiku limene Mulunguyo adatiwombola' (**Aefeso 4:30**).

Zokambirana

1. Kodi ndi cifukwa ciani enaamati mkhalidwe woipa, kusamvelera kapena kugwa kuzabweretsa kuti usakapulumuke? Kodi umakhulupirira kuti cimo lathu kuti 'linga pambanepo' cisomo ca Mulungu?
2. Ngati ncito ikulu ya Mulungu ndi kutitimkhulupirire iye, kodi ndi cotheka kukhulupirira munthu yemwe kuti tsiku lina angatikane?
3. Kambiranani izi: 'ngati tingataye cikhulupiriro izi zinga lepheretse ncito yomwe Yesu adacita pamtanda'.
4. Kodi paliko malemba yomwe yadakukhalisa ndi cidwi cifukwa yaoneka kuti njira ilipo kuti ungataye cipulumutso?
5. Mucipangano cakhale Davide adaphempera musanditaye kundicotsa pamaso panu, musandicotsere mzimu wanu Woyera' (**Masalimu 51:11**). Zi ngakhale bwino kuphemperaphempero iyi mucipangano catsopano?
6. 'Ukapulumutsidwa, nthawi zonse ndiwe wopulumuka' ndi ciphunzitsa cimodzi comwe Akhristu atsutsana naco. Ndi coonadi camthengo kulingana ndi cikondi camuyaya ndi cokhulupiririka pa ife. Kambapo coonadi, izi zitanthauzanji kwa iwe?